

# Malamulo Ochitira Bizinesi

**Corporate Compliance Office**

**+1 919 379 4118**

**Compliance@pyxus.com**

**Pyxus International, Inc.**
**6001 Hospitality Court**
**Suite 100**
**Post Office Box 2009**
**Morrisville, NC 27560**
**United States**
**www.pyxus.com**

**Version 3.1**
**Revised August 11, 2016**
**Updated July 28, 2023**



**Malamulo ochitira Bizinesi**

Pyxus International, Inc.

6001 Hospitality Court

Suite 100

Post Office Box 2009

Morrisville, NC 27560

Phone: +1 919 379 4300

**Nambala yoyimba ulere ya chithandizo***

Malawi

+1-844-539-5353

www.pyxus.ethicspoint.com

**Nambala yoyimba ulere ya chithandizo imayang'aniridwa ndi bungwe la padera.*

# Sitetimenti ya Chilungamo chathu

Alliance One International, Inc. inapangidwa kuti iwone zokhoma za bizinesi za zaka za mu 21st century ndipo ndife odzipereka kukumana ndi zobetchera mopambana ku mbali zonse. Choyambirira cha zimenezo, ndikudzipereka kwathu popanga bizinesi mwa Chilungamo chathunthu.

Kudziwika kwathu kwapadziko lonse chifukwa cha Chikhalidwe chathu chabwino ndi kudalilika pochita bizinesi, kumene kwapangidwa ndi anthu ambiri kwa zaka zambiri, kudzayesedwa ndi kuonedwa mu bizinesi iliyonse imene tikupanga. Tili pa dziko lonse lapansi, mwamphamvu ndiponso timalondola zimene kasitomala wafuna koposa kale. Koma chikhumbokhumbo chopambana ndi kukwaniritsa kasitomala chimayamba ndikutsirizika ndi kudzipereka kwathu potsatila malamulo ndi kuchita mwachilungamo ndipo ngati kampani imene ikupezeka pa dziko lonse lapansi tikuyenera kupanga ndikutsatira malamulo amene akonzedwa a padziko lonse.

M'ndandanda wa malamulo athu wochitira bizinesi ndi umene ukutitsogoza ku mchitidwe wotsatira malamulo moyenera. Ukufotokoza bwino za zimene kampani yikuyembekeza kumbali ya chikhalidwe mokhudzana ndi malamulo ndizoyenera kutsatiridwa ndi wolembedwa ntchito aliyense – chipangano choyenera kutsatilidwa pamene wina walembedwa ntchito. Ma Dayilekitala a AOI, ma Ofisala, antchito ndi wothandizira akuyenera kupanga bizinesi mogwirizana ndi zoyenera kutsatiridwa, chilungamo kumbali ya chuma ndi ndalama.

Tonse timakhala ndi zinthu zimene zimafuna nthawi yathu, koma uthenga umene uli mu m'ndandanda wa malamulo (CBC) udzagwira ntchito ngati mwatenga nthawi ndikuyesetsa kuwuwerenga ndikuchita mobvomerezana ndi ndondomekoyi pochita bizinesi. Ngati mbali ya malamulowa siyikumveka kapena muli ndi mafunso pa zimene mukukumana nazo, mukambirane za madandaulo anuwo ndi bwana wanu, woyimilira depatimenti ya oyang'anira ogwira ntchito, Ofisala wa Corporate Compliance kapena Dayilekita wa Corporate Compliance. Mungathenso kuyimba foni pa nambala yowona za Compliance ya Alliance One kuchokera kwina kuli konse kumene muli pa dziko lonse lapansi kudzera ku nambala ya ulere kapena pa webu sayiti.

Ganizo lakuti maphunziro owona za zoyenera kukwaniritsidwa pochita bizinesi sakuthandizira ku kupambana kwa "zolinga za ndondomekozi"ndi kolakwika. Ngati a AOI, kudzera mukagwiridwe ka ntchito ka ma Dayilekita, ma Ofisala, wogwira ntchito ndi wothandizira pa dziko lonse lapansi, angalephere kukwanilitsa kapena kupitiriza muyeso wa zoyenera kuchita mu ndondomekoyi, kulephelaku kungaononge chuma cha kampani, kupweteka anthu komanso chinthu chofunikira kwambiri cha AOI – dzina lake labwino. Kusunga dzina lake labwino ndi kofunikira kwambiri ku chipambano chathu ndi udindo umene tonse tili nawo.

Tsogolo lathu ndichachidziwikire kuti libweretsa mpikisano ndipo tikuyenera kukonzekera kukumana ndi zobetchera; koma tikuyenera kukonzekera popanda kuchepetsa ndondomeko zoyenera kutsatiridwa zimene zili ngodya za m'mene timachitira bizinesi.



# Zamkatimu

## Poyamba


Zamalamulo athu ........ 1

Malamulo amene akugwira ntchito ........ 2

Kuchotsetedwa kwa Malamulo ena ........ 2

Alliance One International ndi inu ........ 2

Kusabwezera ........ 3

Nambala ya chithandizo ........ 3


## Malamulo

### Kugwira ntchito ku kampani yathu


Za zinsinsi za anthu ........ 4

Kukolana kwa zofuna za munthu ndi kampani ........ 5

Kugulitsa katundu wa kampani ........ 5

Mwayi wa kampani ........ 7

Ziphuphu ndi Katangale ........ 7

Kulipira mphatso, maulendo ndi zosangalatsa za wogwira ntchito m'boma ........ 11

Kupanga ndale ndi Zopereka ........ 13

Kubvomereza/Kupereka mphatso kwa makasitomala ndi ma Sapulaya ........ 13

Kuthandiza osowa ndi kupanga sponsa zochitika zina ........ 14

Kugwiritsa ntchito othandizira a pa dera ........ 14

Kugwira ntchito kwina, Kupanga bizinesi ndi zinthu zobweretsa phindu ........ 14

Kugwiritsa ntchito kompyuta ........ 15

Chinsinsi ........ 15

Zowona za lipoti ya za chuma ........ 16




Kupereka uthenga kwa anthu ........ 16

Chipepeso ndi ubwino wake ........ 17

Kusasalana/Mwayi wosiyana/ Kusazunzana ........ 17

Kuthandiza pa kafukufuku pamene walakwa ........ 18

Kasamalidwe ka Zolembedwa ........ 19

## Kugwira ntchito ku malo athu

Malo a ntchito opanda mankhwala ........ 19

Za umoyo ndi chitetezo ........ 20

Kugwiritsa ntchito ana, Kukakamiza kugwira ntchito ndi Maufulu ena ........ 20

Malamulo a za chilengedwe ........ 20

## Kugwira ntchito ku malo a msika

Kudana ndi kunyanyala ........ 21

Malamulo a boma pa za chinyengo ........ 21

Zoyenera kupereka pamene Kampani yalakwa ........ 21

Kuba ndalama ........ 21

Kudana ndi kusakhulupirika ndi mpikisano wosakondela ........ 22

Ziletso pa malonda ........ 25

Malamulo owona za kutumiza katundu/olowa kapena kutuluka ........ 25

## Potsiriza

Malamulo athu mwa chidule ........ 27



# Za Malamulo athu

Ku AOI, chimodzi mwa zimene timatsatira ndi kudzipereka kwathu ku chilungamo. Mmene timachitira bizinesi ndi mmene timakhalira ndi ena kumaonetsa chithunzithunzi cha Kampani yathu ku dziko lonse lapansi. Ndikofunikira kwa ma sheya hoda athu, makasitomala athu ndi masapulaya, ogwira ntchito athu onse pa dziko lonse la pansi ndi ku madera amene akukhala kuti AOI idziwike ndi chilungamo cha anthu ake ndi kutsata ndondomeko ya bizinesi ya pamwamba.

Khalidwe la zoyenera kutsatiridwa lingathe kutanthauza kutsatira malamulo koposa – koma zikuyamba ndi kutsata lamulo. Mukulimbikitsidwa kuti muthe kudziwa za malamulo mogwirizana ndi dela lanu, maudindo anu ndi ntchito zanu, kuti mudziwe machitidwe ndi zimene mungakumane nazo zimene zingathe kubweretsa mafunso a zoyenera kutsatira ndi pamene mungafune upangiri wokhudzana ndi malamulo. Akulu akulu akuyenera kuwonetsetsa ndi kuthandiza kalondolezedwe ka zoyenera kutsatiridwa mu ndondomeko ya malamuloyi ponena zonse zofunikira za malamulo ndi kuthandiza m'mene onse ogwira ntchito angagwiritsire ntchito ndondomekoyi.

Chitsanzo, ku malo ena ofunikira. Ndondomekoyi ikufotokoza zimene Kampani ikuyembekeza pokhudzana ndi ntchito yanu ndi khalidwe lanu. Ndondomekoyi siyikulongosola za khalidwe lina lililonse limene liri losayenera kapena loletsedwa. Ndiye poti chinthu china sichinatchulidwe sidzikuthandauza kuti ndichololeka mwa lamulo. Kampani ikuyembekeza Dayilekitala aliyense, Ofisala, wogwira ntchito ndi wothandizira pa dziko lonse la pansi kuyesetsa mwa chikhulupiliro pa kumvetsetsa kalata ndi malamulo a AOI ndi malamulo ena ogwira ntchito a CBC.

Sizotheka kukonza vuto liri lonse limene mukukumana nalo. Koma, tikuyenera kuthandizana pa kukhulupirika kwathu pochita bizinesi moyenera ndipo pamene sitikudziwa chochita tikuyenera kufunsa a nzathu kapena odziwa malamulo. Nthawi zina vutolo likhoza kukhala lalikulu kotero ndikofunika uphungu wina wapadera. Dayirekita wa Corporate Compliance (CCD) alipo kuti akuthandizeni. Ngati vutolo silinakambidwe mu ndondomeko ya malamulo ndi udindo wa aliyense kufunsa a bwana ake, nambala ya phoni yothandiza ya Alliance One (wonani "nambala yothandiza" mu bukhuli) kapena Dayirekita wa Corporate Compliance.

Cholinga cha ndondomekoyi ndi kufotokoza bwino lamulo la Kampani ndikupereka CBC ndi ngodya ya Pologalamu ya Compliance ndipo potero ikuyang'aniridwa ndi a CCD. Koma, dipatimenti yowona za Corporate Compliance izagwira nthito limodzi ndi ma dipatimenti ena monga a za chuma, zolemba anthu ntchito ndi kafukufuku ka chuma kuti awone za mafunso ndi madandaulo amene alipo.

Chonde sungani ndondomeko ya malamuloyi pa malo abwino kuti muthe kuyigwiritsa ntchito mtsogolo muno. Zowonjezera za bukhuli zitha kupezeka mosavuta pawebusaiti ya AOI (www.aointl.com) kapena intilaneti ya AOI.



## Malamulo amene akugwira ntchito?

Chifukwa likulu la AOI liri ku Amerika, malamulo a Amerika amafalikira kumalo konse kumene tikugwirako ntchito pa dziko lonse lapansi, ku bizinesi komanso zochita za wogwira ntchito athu kuli konse kumene amakhala kapena kugwira ntchito. Mogwirizananso, mayiko ena angathe kukhala ndi malamulo awo wodutsa malire a maiko awo kwa nzika zawo ndi ma kampani amene ali pansi pa malamulo awo, monga ma bulanchi a AOI.

Nchachidziwikire kuti, malamulo a mumayiko osiyana siyana amasiyana. Nthawi zina pangathe kukhala kukolana pakati pa malamulo a mayiko awiri kapena kuposerapo. Mukakumana ndi mikanganoyi, ndikofunikira kukumana ndi wowona za malamulo wa kampani kapena CCD kuti athe kudziwa mmene angathetsere vutoli bwino bwino.

## Kuchotseredwa malamulo ena

Nthawi zina a CCD akhoza kuchotsapo malamulo ena a CBC iyi potengera momwe zinthu ziriri. Madayilekita ndi mabwana ena akhoza kuchotseredwa malamulo ena a CBC ndi Bungwe la Madayilekita kapena ndi Komiti ya Mabwana Oyendetsa Kampani ndipo zikachitika choncho zidzayikidwa pambalambanda molingana ndi malamulo.

## Alliance One International ndi inu

Mutatha kuwerenga ndondomeko ya malamuloyi, mungathe kukhala ndi funso kapena kukumana ndi mavuto amene mukuwona kuti sanawaunike mokwanira. Kuti mufunse ndikudziwa zambiri zokhudzana ndi malamulo kapena madandaulo okhudza bizinesi, mungathe kulankhula ndi bwana wanu kapena ndi CCD. Wogwira ntchito aliyense; Ofisala, Dayilekitala, kapena wothandizira ndi wobvomerezeka akulimbikitsidwa kuyankhula ndi CCD popanda mafunso ena aliwonse kapena chilorezo chochokera kwa mabwana awo.

Corporate Compliance Director

Alliance One International, Inc.

Telephone: 919-379-4300

Email: compliance@aointl.com

Manijala wowona za Compliance wa mu dera lanu ndi wogwira ntchito wakudera lanu amene angakuthandizeni pa madandaulo ndi mafunso amene mwapereka kwa akuluakulu a kampani, kuphatikizapo zina

Dunnia Chirambo
Local Compliance Manager

Telephone: +265 1 710 044

Email: dchirambo@aointl.com

Wogwira ntchito onse, ma ofisala, ma Dayilekitala ndi wothandizira akuyenera kunena zolakwika zophwanya Malamulo a AOI CBC zimene akudziwa. AOI ili ndi lamulo limene limakutetezani kuti musazunzike ponena mavuto mwachilungamo.

?

### *Kodi Mukudziwa?*

*Pali wogwira ntchito wa mdera lanu amene angakuthandizeni pa zonse zokhudza Compliance mu Chizungu ndi chilankhulo chanu. Mmene mungawapezere a Manijala wowona za Compliance a mdera mwanu yalembedwa ku manja kwa bokosili*

## Kusabwezera

Kampani ikufuna inu mudziwe kuti pamene inu mukuchita bwino, mungathe kufunsa funso liri lonse lokhudza za malamulo kapena ndondomeko zoyenera kutsatiridwa popanda mantha kuti ntchito yanu yingathe kukhala pa chiwopysezo. “Chikhulupiliro cha bwino” sichikutanthauza kuti inu mukhale wolondola –koma chikutanthauza kuti mudzinena zowona ndi mmene mukudziwira. Ngati mukuwona kuti mukukakamizidwa kuti muphwanye lamulo, kapena kuwona lamulo likuphwanyidwa, muyiwuze kampani. Ndikulakwira mndandanda wa malamulo pamene Dayilekitala, Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira apereka chilango kwa iye amene aulula zophwanya china chiri chonse mu mndandanda wa malamulo. Dayilekitala, Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira amene apereka chilango kwa omwe aulula zophwanya malamulo adzapatsidwa disipulini ndipo angathe kuchotsedwa ntchito.

## Nambala ya chithandizo

Kuwonjezerapo, ngati mukufuna musadziwike, mungathe kupereka mafunso kapena madandaulo poyimba **nambala yoyimba ulere** ya Alliance One, yosavuta kwa inu, yimagwira kwa maola 24 pa tsiku, masiku asanu ndi awiri pa sabata, kuti mufunse mafunso, mupereke madandaulo a mu ndondomeko yowona za bizinesi ya Alliance One, kuphatikizapo kuwerengera ndalama za kampani mwachinyengo kukhazikitsa njira zotetezera chuma, zokhudza kafukufuku wa mabuku  a ndalama.

Mukulimbikitsidwa kubweretsa madandaulo anu ku kampani ndipo mungachite izi posapereka dzina lanu. Sipasungidwa mbiri ina iliyonse kapena chida chimene chingapange kalondolondo wa nambala ya foni yimene mukuyimbira. Mukayimba pa nambala yothandiza, mudzalumikizidwa ndi wothandizira amene amawona za nambalayi. Katswiri wa zoulutsa nkhani amagwira ntchito ku kampaniyi, osati Alliance one adzakuthandizani. Ku madera ambiri katswiri wa zoulutsa nkhani amayankhula chilankhulo cha ku malo amenewo.

Katswiri wa zoulutsa nkhani adzakupatsani moni ndikufunsa mmene angakuthandizireni. Mukapereka chifukwa choyimbira foni, uthenga wanu adzausonkhanitsa katswiriyu kuti athe kumvetsetsa chifukwa chimene mwayimbira foni. Adzakupatsani nambala ndikugwirizana tsiku lodzakuyimbirani.

Muli olimbikitsidwa kugwiritsa ntchito Nambala yaulere ya compliance popereka nkhawa ndi mafunso anu. Alliance One siyingafikire mlingo woyendetsera bizinesi wa pa mwamba zimene zili mu ndondomeko ya malamulo popanda chithandizo chanu.



?

*Kodi Mukudziwa?*

***Nambala yoyimba ya ulere** ya compliance imayang'aniridwa ndi anthu apadera ndipo mungathe kupereka uthenga mobisa, ngati mukufuna pa foni  kapena pa intaneti.*

## Za chinsinsi za anthu

Nambala yothandiza ku Malawi mukhoza kuipeza poyimba 704 5 542 198. Ndondomeko zimene zikuyenera kutsatiridwa   poyimba foniyi zayikidwa pa bolodi ku maofesi ndi mafakitale onse a Alliance One komanso zikupezeka mu Chizungu komanso mu zilankhulo za deralo kuchokera kwa ma Manijala a Compliance**.** Poonjezera nambala yothandiza kasungidwe ka malamulo ingathe kupezeka paintaneti pa aoicompliancehelpline.alertline.co

Lipoti lidzakonzedwa ndi kampani ya padera imene imawona za Nambala yothandiza, ndipo  lidzatumizidwa kwa CCD wa Alliance One. CCD adzaunika vutolo, kuyankhula nanu, ngati kuli kofunika ndi kuyambitsa kafukufuku. Ngati mwapereka Nambala yanu, CCD adzakuyimbirani ngati kuli kofunika. Ngati mwasankha kuti musadziwike, kampani imene imawona za nambala yothandiza idzawuzidwa  za zotsatira za kafukufuku kuti akuyankheni pa tsiku limene mwagwirizana.

## Kugwira ntchito ku kampani yathu

Ndi lamulo la Kampani kuteteza mwamphamvu zinsinsi za wogwira ntchito. Choncho:

- Mu kuyenera kutsatira malamulo owona za chinsinsi ndi malamulo oteteza zopezeka pa kafukufuku, malamulo ndi mgwirizano. Mwa chitsanzo, malamulo a chinsinsi a ku Amerika makamaka amene akuwona zotchinjiriza anthu kumbali ya chipatala, chuma, ndi uthenga wa ogula ndi uthenga wokhudza ana. Lamulo lowona za chinsinsi la European Union liri ndi chitetezo cha chipatala ndi umoyo, uthenga wowona zoulula mtundu wa munthu, za ndale, za mipingo ndi zikhulupiliro, membala ku bungwe la anthu ogwira ncthito, kapena uthenga wowona za  zogonana za munthu.

- Chifukwa choti malamulo owona za kuteteza zinsisi ndi ambiri,   komanso ovuta kuwamvetsetsa, mukuyenera kufunsa woona za malamulo a pa Kampani musanakhazikitse kapena kusintha mulu wa chiwerengero wosungidwa mu kompyuta kapena zina zimene kampani imatolera, kugwiritsa ntchito, kapena kulengeza za chuma cha munthu, thanzi kapena za chipatala, mtundu, za ndale, za mpingo ndi   zikhulupiliro, membala ku bungwe la anthu a pa ntchito, kapena umoyo wa  m'banja ndi nkhani zina zobisika za munthu.

- Mwalamulo, ngati kampani ili ndi chinsinsi cha munthu, ndi lamulo la kampani kuti chigwiritsidwe ntchito moyenera komanso pazinthu zokhazo zomwe ndi zovomerezeka komanso osawulula chinsinsicho pokhapokha ngati zili zololedwa ndi malamulo, mutalandira uphungu kwa Mkulu Wodziwa za Malamulo wa kampaniyi kapena CCD. Komabe, zokambirana zapamakina amagetsi zolembedwa pogwiritsa ntchito makina a kampani sizachinsinsi ndipo AOI ili ndi ufulu, molingana ndi malamulo, kugwiritsa ntchito zokambirana zonse zomwe zinalembedwa kapena kusungidwa pogwiritsa ntchito makina



## Za chinsinsi za anthu (Kupitiliza)

a kampani. Zina zowonjedzera zokhuzana ndi malamulo a kampani pa zinthu zachinsinsi zili pa intraneti.

- Mukuyenera kufunsa kaye kwa Mkulu Wodziwa za Malamulo wa kampaniyi kapena CCD musanapange lamulo lililonse lachinsinsi kaya ndiloti ligwiritsidwe tchito pa internet kapena ayi komanso mutsatire malamulo onse.

## Kukolana kwa zofuna za munthu ndi Kampani

Kukolana kwa zofuna za munthu ndi kampani kumachitika pamene zofuna zamunthu zikuwoneka kuti zikukhulana ndi zochita za kampani. Kukolanaku kungathe kukula ngati Dayilekitala, Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira apanga zinthu zimene zingapangitse kugwira ntchito kwake bwino bwino kuti kusokonezeke. Mkangano ungakhalepo ngati Dayilekitala, Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira kapena a pa banja lake alandila ma benefiti molingana ndi ntchito yake ku kampani. Kugulitsa masheya, kuphumitsa kampani mwayi wa bizinesi, kupanga bizinesi ndi zina mwa zinthu zomwe zingapangitse kuti pakhale kukolana pakati pazofuna zanu ndi zakampani.

Zinthu zomwe zingapangitse kuti pakhale kukolana zikuyenera kunenedwa polemba kalata kwa CCDCCO kapena CLO komanso mapepala ake onse akuyenera kuperekedwa molingana ndi malamulo.

Kukhala ndi zinthu zopangitsa kuti pakhale kukolana sikuswa malamulo athu akagwiridwe ka ntchito koma kulephera kunena ku kampani za zinthuzo.

## Kugulitsa Katundu wa Kampani

Pochita bizinesi ya AOI, mungathe kupeza zinsinsi za kampani zimene sizikuyenera kudziwika kwa anthu ogula masheya ("uthenga wosafunika kudziwika kwa anthu"). Mukuyenera kusunga chinsinsichi ndipo musachigwiritse ntchito mogwirizana ndi kugula kapena kugulitsa masheya a kampani kapena zinthu zina zimene zikugwirizana ndi zogula kapena kugulitsa kapena kugwiritsa ntchito pomunong'oneza wina.

Malamulo amayiko ambiri makamaka, Amerika, akuletsani kugula kapena kugulitsa katundu wa kampani pamene muli ndi uthenga umene sukuyenera kudziwika ndi anthu ena. Pansi pa malamulo a kampani komanso malamulo a dziko la Amerika, uthenga umakhala wofunika ngati:

- Nchachidziwikire kuti wogula angathe kugwiritsa ntchito uthengawo pamene akusinthasintha zogula masheya a kampani; kapena
- Uthengawu ngati ungalengezedwe kwa onse, utha kukhudza mtengo wa masheya a kampani.

Malamulo amayiko ambiri makamaka Amerika, akuletsa kugula kapena kugulitsa katundu wa kampani pamene muli ndi uthenga umene sukuyenera kudziwika ndi anthu ena. Pansi pa malamulo a kampani komanso malamulo a dziko la Amerika, uthenga umakhala wofunika ngati: Uthengawu ungathe kukhala wofunika angakhale ukukhudza za mtsogolo, mpheketsera kapena zochitika za mtsogolo kapena wofunikira pokha pokha ngati zalengezedwa kwa anthu. Uthenga wofunika ukhoza kukhala wabwino kapena woyipa. Nkhani yachinsinsi ikhonza kukhala yofunika angakhale ku ma kampani amene sagulitsa masheya, ali ndi ma bondi kapena ngongole za ku banki. Choncho, powona zimenezi, uthengawu ukhoza kukhala wofunika komanso ndiosafikira:

### Kodi Mukudziwa?

*Pamene mukugwira ntchito, mungathe kupeza uthenga umene simukuyenera kugwiritsa ntchito kapena kugulitsa. Kuti mudziwe zambiri za "kugulitsa za mkati" wonani malamu a kampani owona zogulitsa za mkati amene angapezeke pa intaneti.*

Wotheka ndi wowona

- Zolengeza chiongola dzanja kapena zongoyerekeza, kusintha, zimene zinalengezedwa kale kapena zongoyerekeza;
- Zotsatira za chuma;
- Zolembedwa ndi zowonjezeredwa ku ngongole zamgonagona;
- Kukuza kapena kuchepetsa magwiridwe a ntchito;
- Katundu wa tsopano, zopangidwa ndi zozindikiridwa mwatsopano;
- Milandu yayikulu kapena zochita za boma
- Kuphatikizana zogulidwa, zonenera malonda, kugwirira ntchito limodzi ndi makampani ena kapena zosintha ku katundu wa kampani;
- Zosintha pa zimene akatswri ayamikira kapena mlingo wa ngongole; Zichitochito zokhudza ma sheya a kampani (monga kulephera kwa kubwezera ma sheya, kuitanira ma sheya ogulitsidwa kuti kampani iwagulenso, mapulani ogulanso katundu wogawidwa, kusintha kwa cholowa, kusintha kwa umwini wa ma sheya;
- Kusintha kwa oyendetsa kampani ndi njira zatsopano zokhudza kayendetsedwe ka kampani;
- Kubwereka ndalama kopitiriza muyeso;
- Vuto la kapezedwe ka ndalama
- Zosintha za ma Auditor kapena chidziwitso cha kampani chochokera kwa Auditor kuti kampani siyingadalirenso lipoti ya Auditor.

Musagulitse katundu wa kampani ndi katundu wina aliyense pamene uthenga wosafunika kudziwika usanalengezedwe kwa anthu. Ziletsozi zikuphatikizapo zoletsedwa za mu pulani ya kampani 401(k), monga zosankha zopereka chithandizo za mtsogolo kapena ma balansi a ma akawunti akale amene akubwera chifukwa chogulitsa kapena kugula (pofuna kapena kusafuna) katundu wa AOI. Powonjezera, chisankho chogula katundu ndicholetsedwa ngati ukupanga uli ndi nkhani yosafunika kuti udziwike ndi anthu.

Ngati uthenga wosabisikawu ukhudzana ndi kampani ina (pophatikizana mwa chitsanzo) simungagulitse katundu. Powonjezera ku zogula pamene uli ndi uthenga wosafunika kuti udziwike ndi anthu, ndi kuswa lamulo ndi kuphwanya lamulo loona za malonda la Insider Trading Policy komanso mndandanda wa malamulo kupereka uthenga kwa amene mukudziwa kuti sawugwiritsa bwino ntchito uthengawu pogula katundu wa kampani kapena popereka uthengawu kwa amene akuchita malonda. Izi zikukhudza ngakhale wopereka uthengawu akukhudzana ndi wamkati

mochita malondawa monga trust kapena kampani ndipo ngakhale mulandire ndalama kwa opereka uthengawu. Aliyense amene aphwanye malamulowa adzachotsedwa ntchito, adzapereka fayini ya ndalama ndi kumangidwa. Uthenga udzatchedwa wodziwika kwa "anthu" onse pa tsiku la chitatu lamalonda uthengawu utalengezedwa ndi ofisala woyenera wa kampani. AOI, ma Dayilekitala, ma Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira adzatengedwa ngati olakwa ndi kutha kumangidwa pophwanya malamulo ogulitsira malonda. Ma Ofisala, wogwira ntchito ndi wothandizira amene akuphwanya lamuloli adzaweruzidwa, kuwonjezerapo kuchotsedwa ntchito. Komanso, Dayilekitala adzawuzidwa kuti asiye ntchito

Kuti mudziwe zambiri, chonde wonani za lamulo ka kampani la *Insider Trading Policy*, kapena funsani wamkulu wowona za Malamulo wa kampani

## Mwayi wa Kampani

Ma Dayilekitala, ma Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira akuletsedwa kugwiritsa ntchito mwayi kapena kuwupereka kwa ena umene aupeza pogwiritsa ntchito katundu wa kampani, uthenga kapena udindo popanda chilolezo cha bodi. Ma Dayilekitala, ma Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira sakuyenera kugwiritsa ntchito katundu, uthenga, kapena udindo wawo popeza zinthu zawo mopikisana ndi Kampani mu njira ina iliyonse. Ma Dayilekitala, ma Ofisala, wogwira ntchito kapena wothandizira akuyenera kuchita mwa chilungamo pamene apeza mwayi. Yankhulani ndi a CCD kuti akulangizeni.

## Ziphuphu ndi Katangale

Ziphuphu ndi kuswa malamulo. Zimaononga madera amene tikugwirako ntchito. Tikuyenera kutenga nawo mbali pa njira zothandiza kuthetsa ziphuphu. Aliyense wa ife ayenera kutsatira malamulo onse odana ndi ziphuphu. Awa ndi malamulo a dziko limodzi amene amaletsa katangale mu mayiko ena. Sitikuyenera kupereka ziphuphu mu njira iliyonse, kuphatikizapo:

- "Mphatso" zoperekedwa- ngakhale zili zochepa.
- Zopereka kuti mukonderedwa povomerezedwa kuchita zinthu, msonkho kapena kasitomu, ziphaso; zovomerezeka kapen zina.
- Zopereka kwa amene tikupikisana nawo kuti apereka uthenga wa chinsinsi
- Zopereka ma commission mwa chiphuphu
- Zopereka kwa makasitomala ndi zosavomerezeka
- Malipiro kuti mukonderedwe ndi opereka ngongole, monga ngati ma banki.

Ngakhale ziphuphu ndi kuswa Malamulo ndikulakwira Malamulo a kampani, chiphuphu chitaperekedwa kwa wogwira ntchito m'boma kapena munthu wamba, kasitomala kapena sapulaya, wogwira ntchito ku Alliance One akuyenera kudziwa zimenezi.



*Kuchita ziphuphu ndi anthu ena*

Lamulo la U.S. Foreign Corrupt Practices Act ("FCPA") limati ndikuphwanya lamulo ngati kampani yaku U.S., ngati AOI, kapena mabulanchi ake, wothandizira, wogulitsa pa mbali pa kampani ndi ena ndi wogwira ntchito, kupereka kapena kulonjeza kwa wogwira ntchito m'boma poyembekeza kulandira kapena kuti iyeyo adzapangitsa chisankho chopanga bizinesi ndi kampani. Izi zingathandize kupeza bizinesi ya tsopano, kusunga yakale kapena kukonderedwa.

Lamulo la FCPA limakakamiza dipatimenti ya za malamulo a U.S. Department of Justice ("DOJ") komanso owona za malamulo okhudza anthu a U.S. Securities and Exchange Commission ("SEC"). FCPA ili ndi mbali ziwiri: (a) malamulo odana ndi ziphuphu ndi (b) malamulo owona za kayendetsedwe ka ndalama.

(a) Malamulo odana ndi ziphuphu a FCPA amaletsa kupereka mwachinyengo kwa wogwira ntchito m' boma. Zimene ziri mu malamulo odana ndi ziphuphu za mu FCPA ndi:

- Kupereka, kapena kulonjeza china **chiri chonse chofunikira**
- Kwa **wogwira ntchito m'boma** aliyense, kapena aliyense amene sali wachipani kapena wa chipani ku U.S., woyimilira boma kunja akudziwa kuti mbali yandalama kapena lonjezo lidzaperekedwa kwa mmodzi wa anthuwa;
- Cholinga **chofuna kupanga katangale** pofuna kuchititsa chiganizo, kupangitsa munthu kuchita kapena kuphwanya lamulo, kupangitsa munthu kuchititsa boma kupanga chinthu kapena, chiganizo; Zochita za katangale pofuna kukopa kapena chisankho, kupangitsa munthuyu kulakwa pa ntchito yake, kuti agwiritse ntchito mphamvu zake ku boma la kunja kuti apangitse chisankho cha boma;
- Pothandiza **kupeza ndi kusunga bizinesi** ndi kapena, popereka bizinesi kwa munthu kapena kampani.

?

*Kodi mukudziwa?*

*Malamulo a kampani amaletsa kupereka kapena kulandira ziphuphu ngakhale kuti munthu amene akulandira kapena kupereka chiphuphu ndi wogwira ntchito m'boma kapena ayi.*



# Ziphuphu ndi Katangale

?

*Kodi Mukudziwa?*

*Powonjezera pa ziphuphu kukhala zoletsedwa, ndikolakwika kusokoneza chuma cha kampani mu mabuku ndi zolembedwa*

“China chili chonse chimene chili chofunika” chikufotokozedwa motambasulidwa”. Powonjezera ndalama, ma benefiti ku achibale ndikupeleka ma benefiti kwa munthu wina. Zitsanzo ndi:

- Ndalama zofanana ndi ndalama, kapena ma benefiti (ma travelling cheque ndi ma benefiti);
- Ntchito zopanga munthu yekha;
- Ntchito kapena kupatsidwa
- Kuthandiza wosowa ukudziwa kuti upindulepo;
- Zopereka kundale ; ndi
- Kugwiritsa ntchito katundu wa kampani (kuphatikizapo ndege, nyumba, magalimoto, maboti. Ndi zina zotere.) ndi wogwira ntchito m’boma kapena a ntchito awo kuti atukule ndi kuwonetsa katundu wa kampani ndi ntchito zake.

(b) Malamulo a FCPA akufuna kuti makampani azisunga mabuku a za chuma ndi mbiri ya zochitika za bizinesi zisungike bwino komanso kuonetsetsa kuti njira zoonetsetsa kuti ndalama sizikuonongeka. Izi zakhazikitsidwa kuti zichepetse ndalama zosawerengedwa ndi zina zolipira zosadziwika bwino zimene zingakhale njira zopelekera ziphuphu kubisa chifukwa cholipilira.

Kuphwanya malamulo a FCPA kapena malamulo odana ndi ziphuphu kudzapangitsa kuti mumangidwe, mulipire fayini ndi zilango zina. Mwa chitsanzo, anthu adzapatsidwa fayini yokwanira $250,000 USD ndi kumangidwa kwa zaka 5 polakwira malamulo odana ndi ziphuphu, polakwila malamulo ama akawunti adzapatsidwa fayini yokwanira ndikumangidwa kwa zaka 20. Powonjezera, kampani idzazengedwa mlandu ndi kulipira fayini ndi zilango zina. Opanga bizinesi amene sakulemekeza malamulowa sakutetezedwa. Wogwira ntchito aliyense ameme akonza mphatso, kupereka ndi kulonjeza kupereka zinthu zofunikira adzaphwanya lamuloli ndipo adzalangidwa ndi kampani, ndipo adzachotsedwa ntchito.

FCPA ikugwirizana ndi mphatso,kupereka ndi kulonjeza kwa ogwira ntchito kapena amene sanalembedwe ndi kampani. Motero, FCPA ikuti ndikuphwanya lamulo “kuyang’ana mwa njira yina” zinthu zimene zikuwonetsa kuti munthu akuphwanya malamulo popereka mphatso, kupereka kapena kulonjeza kupereka moyimilira kampani. Powonjezera, kupereka ndalama kwa munthu wapadela ndi cholinga chakuti iyeyu apereke mphatso, kupereka kapena kulonjeza kupereka kapena kunyozera lamuloli ndikuphwanya lamulo.

**Wogwira ntchito m’ boma ndi ndani?**

Chifukwa cha malamulo a kampani, tanthauzo la “wogwira ntchito wa boma”ndi wogwira ntchito poona za kasitomu ndi za olowa m’dziko, wosankhidwa kuona za malamulo, Meya, Nduna ya boma ndi wogwira ntchito ena a m’boma ma Ofisala kapena wogwira ntchito ku mayiko a kunja monga a United Nations, World Bank kapena International Monetary Fund; oona za

makampani a fodya monga ma insipekitala a za malimidwe; akulu kulu andale ndi oyimilira ma udindo a zipani.

**Zofunikira wogwira ntchito wonse pa udindo wina uli wonse kapena owona zokhudza fodya ndi wogwira ntchito aboma**. Izi zikukhudza makasitomala komanso:

- Global Tobacco Ltd.
- Imperial Vina Danang
- Japan Tobacco, Inc.
- Khanh Hoi Cigarette Factory
- Tian Li International Co. Ltd.
- Vietnam National Tobacco Corporation
- Fabrika Dunhana Sarajevo, Bosnia & Herzegovina
- Societe Nationale des Tabacs et Allumettes
- China Tobacco International Inc.
- Eastern Company S.A.E.
- National Tobacco Enterprise
- Sekap, S.A.
- Korea Tomorrow and Global Corp.
- Iran Tobacco Company
- Regie Libanaise des Tabacs et Tombacs
- Libyan Tobacco Company LTC
- Taiwan Tobacco & Liquor Corporation
- Thailand Tobacco Monopoly
- Regie National des Tabacs et des Alumettes
- Manufacture des Tabacs de Kairouan
- Vietnam Tobacco Import & Export Co
- National Cigarette and Match Industries Ltd.
- Saigon Tobacco Company
- Thang Long Tobacco Company
- Saigon Industry Corporation
- Khatoco

Izi ziKuthawuza chani? Izi zikutanthawuza kuti aliyense amene akugwira ntchito m'boma kuyambira Nduna yayikulu mpaka woperekera makalata ndi "wogwira ntchito m' boma" pa malamulo a kampani. Wogwira ntchito ku khoti, ma jaji, ma kalaliki ndi ena otere ndi wonse wogwira ntchito m'boma" pansi pa malamulowa. "Wogwira ntchito m'boma"kuphatikizapo achibale awo ndi ena amene amatha kulandira zinthu zofunikira zimene zaperekedwa kuti apereke ma benefiti kwa wogwira ntchito m' boma.

Ngati muli ndi mafunso okhuza malamulo odana ndi ziphuphu, muyankhule ndi a CCD



**Mphatso, Kuyenda ndi zisangalalo za wogwira ntchito m'boma.**

FCPA ikuletsa kupereka "zinthu ziri zonse zofunikira" kwa ogwira ntchito akunja **kwa dziko** pokha pokha patakhala ndondomeko yololedwa ndi malamulo.

**Mphatso:** Simungapereke mphatso kwa wogwira ntchito m'boma kuti akondere kampani pamene pali mpikisano. Mphatso ina ili yonse imene yaperekedwa kwa wogwira ntchito m'boma ikuyenera kugwirizana ndi lamuloli. Zinthu izi zikuyenera kutsatidwa: (i) mphatso za ndalama kwa wogwira ntchito m'boma ndizosavomerezedwa; (ii) mphatso zazing'ono zing'ono zimene ziri ndi logo ya kampani zingaperekedwe kwa wogwira ntchito m'boma pomuthokoza kapena kumupanga kuti amve kuti walandiridwa; (iii) mphatso zikuyenera kukhala zogwirizana ndi katundu ndi nthawi yimene zapelekedwa; ndi (iv) mphatso zake zikuyenera kuvomerezedwa ndi lamulo la boma. Mukuyenera kulandira chilorezo chochokera kwa CCD musanapereke mpatso kwa ogwira ntchito m'boma, izi zikuphatikizapo makasitomala. Mphatso zikuyenera kuwunikidwa mogwirizana ndi *lamulo lowona za zowonongedwa popereka mphatso.*

**Ndalama zimene zagwiritsidwa ntchito Poyenda**: Ngati malipiro mmalo mwa kampani poyenda ndikulipira kumalo kumene wogwira ntchito boma akukhala (kuphatikizapo makasitomala athu) zikuyenera kuvomerezedweratu ndi a CCD. Izi zikuyenera kutsatidwa: (i) ndalama zokhazo zimene zagwira ntchito pamene munthu wayenda pochita bizinesi ya kampani ndiye zizabwezedwe; (ii) ndalama yolipira ndege ya (osati ya first class) siyizabwezedwa; (iii) kampani siyizasankha wogwira ntchito m'boma woti ayende (koma boma likuyenera kutero kapena kasitomala wa AOI; (iv) Wogwira ntchito okhawo ndi amene azabwezeredwe zimene awononga koma za abale awo sizidzabwezedwa.

**Chisangalalo nthawi ya Bizinesi:** Simukuyenera kusangalatsa wogwira ntchito m'boma (kapena kupereka chisangalalo) ngati mukudziwa kuti chisangalalocho chipereka mwayi ku kampani. Bizinesi kapena chisangalalo chimene chingasangalatse makasitomala athu ang'onoang'ono sichingathe kusangalatsa makasitomala athu a akuluakulu (wogwira ntchito m'boma). Chisangalalo cha wogwira ntchito m'boma ndi chovomelezeka pokha pokha (i) chikugwirizana ndikutukula, kulongosola ndi kuwonetsa bizinesi ya kampani; (ii) chigwiritsa ntchito ndalama zochepa; (iii) chovomerezeka ndi malamulo; (iv) chogwirizana ndi makhalidwe a kuderalo; ndipo (v) chikupewa zonse zimene zingapangitse kuti chisawoneke bwino. Ngati mukukayikira kuti chisangalalochi chigwiritsa ntchito ndalama zambiri wuzani a CCD.

*i*

*Kuti Mudziwe Zambiri*

*Ngakhale Mbali iyi ikuwona zolipira za mayendedwe ndi chisangalalo cha wogwira ntchito M'boma, Malamulo a kampani okhuza mayendedwe ndi chisangalalo a dziko lose lapansi akufotokoza*

Mukuyenera kuwonetsetsa nthawi zonse kuti mphatso, kuyenda kapena zisangalalo zoperekedwa kwa wogwila ntchito m'boma zikugwirizana ndi malamulo a kampani angakhale pali za chikhalidwe ndi zochitika za ku deralo.

**Kuthandizira kapena kupereka ndalama "zochuluka":** Mu mayiko ena wogwila ntchito m'boma amayembekezera kupatsidwa ndalama zochuluka kuti athandize kumbali ya boma. Zopereka zoterozo ndizovomerezeka pokhapokha:

- Zoperekedwazo ndizochepa;
- Ndalama zoperekedwazo zikufuna kuti boma lichitepo kanthu ndipo kampani ikukwaniritsa zonse za boma; ndipo
- Zoperekazo simbali ya zopereka zina zakale;ndipo
- Zoperekedwazo zikugwirizana ndi malamulo a muderalo, malamulo, ndi zochitika kapena palibe chimene chingachitike kuti mupangitse boma kuti lichitepo kanthu.

Chofunikira kwambiri, ngakhale zoperekazi zitha kuvomerezedwa ndi a FCPA, sizingakhale zovemerezedwa mumalamulo a mayiko ena, kuphatikizapo dziko limene zoperekazi zikuperekedwa. Lamulo la UK Bribery Act, lamulo la O.E.C.D. Anti-Bribery Convention ndi ena. Potero, zoperekazo zikuyenera kuchitika pokha pokha ngati zavuta. Ngati kuli kotheka, ngati mukudziwiratu, kalata yachibvomerezo itengedwe kwa a CCD.

Powonjezela, ngati zoperekazi sizingapeweke, ndikoyenera ndi kwa bwino kuti zoperekazi zilembedwe m'mabuku a kampani. Zolembedwazi zikuyenera zilembedwe bwino bwino osati kubisidwa. Ngati muli ndi mafunso okhudza kaperekedwe ka ndalamaka, funsani a CCD a AOI.

## *Kuti Mudziwe Zambiri*

*Kuti mudziwe zambiri za zopereka ndi zina zokhudza compliance, wonani ma video pa intaneti pamene akukamba za compliance. Mungapeze njira yowonera zambiri za zimenezi pamene akukamba za AOI.*



# Ziphuphu ndi Katangale

### *Kuti Mudziwe Zambiri*

*Mbali iyi ya malamulo ochitira bizinesi ndi kampani a CCO ndi CCM a kampani ndi wokuthandizani kuti mumvetsetse pamene pali poyenerela kupereka mphatso. Kuti muthandizidwe kumvetsetsa mmene mungaperekere mphatso. Wonani Malamulo a kaperekedwe ka mphatso a padziko lonse lapansi.*

**Kupanga ndale ndi zopereka**

Wogwira ntchito paokha akulimbikitsidwa kupanga nawo ndale. Mukuyenera kusaphatikiza kampani pothandizira oyimira ndale kapena zina zokhudza ndale. Musagwiritse ntchito dzina la kampani mogwirizana ndi za ndale. Kampani siyidzapereka ndalama kwa wogwira ntchito pamene iye wapereka zopereka ku ndale.

Pamene mukuyimira kampani, mukuyenera kutenga nawo mbali mu ndale zosakondela monga mwauzidwa ndi a Chief Executive Officer. Ngati mwasankhidwa kutenga nawo mbali mu kampeni pamene mukuyimira kampani, mukuyenera kusamala kuti musapange nawo kampeni. Kampeni imakhala pansi pa malamulo a dziko ndipo imafuna zambiri. Ngati muli ndi mafunso okhudza zochitika za ndale, funsani a CCD a AOI.

*Madandawulo a Ziphuphu a ena*

**Kuvomereza / kupereka mphatso kwa makasitomala ndi ogulitsa katundu**

A AOI siyikufuna bizinesi yopanga mwachinyengo. Mukuyenera kuziyikapo mtima zimenezi. Ngati Dayilekitala, Ofisala, kapena wothandizira, mukuyenera kugwira ntchito mogwirizana ndi ziyang'aniro za kampani. Izi zikutanthauza kuti musalole zolinga zanu kukolana ndi udindo wanu woyimilira zolinga za kampani. Mukuyenera kugwiritsa ntchito bwino chiganizo chanu, koma dziwani izi.

Pogwira ntchito ndi makasitomala mungalandire kapena kupereka mphatso zochepa polemekezana kapena kulimbikitsa ubale. Koma, NDALAMA NDIZOLETSEDWA. Zina zoletsedwa ndi:

- Ngongole ziri zonse pokha pokha ngongole za kuma banki pamene mukuchita bizinesi;
- Zakudya, zakumwa, zisangalalo, kuyenda ndi kugona, kapena kulipira zimenezi, pokha pokha ngati mwini wakeyo alipo, ndipo zikukhudzana ndi bizinesi.

Mukuyenera kusamala povomereza mphatso; mukuyeneranso kusamala popereka mphatso ndi cholowa kwa amene mukuchita nawo bizinesi.

Kampani ikuyembekeza inu kuti mupange ma ubale a mphamvu. Izi zifuna chidwi chanu ndi kudzipereka kwanu. Musapereke mphatso za mtengo wodula kwa ma sapulaya, makasitomala, ndi ena amene mukupanga nawo bizinesi ndipo iwo asayembekezere izi kuchoka kwa inu. Mphatso, kukondera, ndi chisangalalo chingaperekedwe ku ma phwando ngati;

- Zikugwirizana ndi bizinesi;
- Zosadula ndipo sizitengedwa ngati ziphuphu;ndipo
- Zikugwirizana ndi lamuloli ndi malamulo ena ndi zimene zikuyenera kutsatiridwa.

Pakuti malamulo ambiri akuwona za mphatso za pa dera, nkofunikira kuwuza a CCD a kampani popereka kapena kulandira mphatso.

## Kuthandiza osowa ndi ku kupanga sponsa zochitika zina

Ngakhale pamene mukuchita ubwino, kuthandiza osowa ndi kuthandizira zochitika zina ndikovuta chifukwa cha ubale pakati pa wolandira chithandizochi ndi wogwira ntchito m'boma. Zovuta zina ndi zokhudza zopereka ndi kuthandiza kasitomala kapena boma. Izi sizikukhudza ngati wolandira chithandizoyo ali wa boma kapena ayi. Potero, zopereka zonse zothandiza anthu osowa zikuyenera kuvomerezedwa ndi a CCD.

## Kugwiritsa ntchito othandizira apadera

Nthawi zina ndikofunikira kugwiritsa ntchito munthu wa pa dera kuti akuthandizeni pochita bizinesi ya kampani. Kampani siyikufuna kugwira ntchito ndi othandizira amene akuphwanya malamulo ena onse ndi CBC ndi malamulo ena.

## Kugwira ntchito kwina, Kupanga bizinesi ndi zinthu zina zobweretsa phindu

Nthawi ndi nthawi mukhoza kupeza mwayi woti mugwire ntchito kwina, kupanga bizinesi kapena zinthu zina zobweretsa phindu zomwe sizokhudzana ndi Kampani. Ngati zitakhala choncho mukuyenera kutsatira malamulo awa.

Kugwira ntchito kwina kapena kupanga bizinesi yomwe siyikukhudzana ndi kampani ndikololedwa bola ngati sizikukolana ndi udindo womwe muli nawo kapena kagwiridwe kanu ka ntchito ku Kampani. Ntchito kapena bizinesi yina yili yonse yomwe yili ndi phindu la chuma yomwe yikupikitsana ndi Kampani yikuyenera kunenedwa kwa kapitawo woyang'anira ntchito komanso CCD, komanso mapepala onse okhuza ntchitoyo kapena bizinesiyo akuyenera kuperekedwa molingana ndi malamulo a Kampani. 'Phindu lachuma' ndi phindu

lina lililonse la chuma lomwe lingapangitse kuti musapange chigamulo cholondola chokhudzana ndi ntchito yanu.

Mukulimbikitsidwa kutenga nawo mbali pa ntchito zachifundo, za akatswiri kapena zamabungwe othandiza anthu bola ngati sizikusokoneza kagwiridwe kanu ka ntchito ku AOI. Kuwonjedzera apo, ngati mukuganiza kuyamba bizinesi yina yili yonse yomwe yingakolane ndi ntchito ya kampani, muwauze a CCD.

## Kugwiritsa ntchito sofutiweya ya kompyuta

Kukopera ma sofuti weya a weniwake ndikuphwanya malamulo a kampani ndi malamulo a zokopera, ndipo zingapangitse kampani kuti iphwanye malamulo a wosindikiza ma sofuti weya. Kuletsaku ndi kwa aliyense osatengera dziko, malo kapena zikhalidwe za mu dera lawo.

Aliyense wa ife ali ndi udindo woonetsetsa kuti katundu wa kampani ndi zinsinsi zonse zikugwiritsidwa ntchito popanga bizinesi ya kampani pokha. Musagwiritse ntchito katundu wa AOI pogwira ntchito zanu zimene sizikugwirizana ndi bizinesi ya kampani popanda chilorezo.

## Ya Chinsinsi

“Katundu” akuphatikizapo zinthu ndi zomangidwa. Uthenga umene mumapanga pogwira ntchito ndi “za kampani”--- ndiye kuti, ndi katundu wa mtengo wa patali wa kampani. Uthenga ungathe kukhala ndi za chinsinsi, chuma, ntchito, ma pulani a bizinesi, ma dokumenti, kapena ma databesi. Uthenga uliwonse wokhudza makasitomala athu, udzatengedwanso ngati “wa kampani” ndipo ndi zinsinsi. Chonde dziwani kuti zinsinsi zathu zimasungidwa mu makina. Mukuyenera kutchinjiriza uthenga umene wasungidwa mumakinawa mmene mungasungire pepala lina liri lonse lofunikira.

Musamale osagawana uthenga wa chinsinsi wa kampani ndi ena, kuphatikizapo wogwira ntchito, pokha pokha ngati zili zokhudza bizinesi.  Uthengawu utatulutsidwa ungathe kuwonongeka ndikupweteketsa ena. Kumbukiraninso kuti kuwulura uthengawu (mwa chitsanzo, pa ma foni, malo amene muli anthu, mu ndege, ma eleveta, malo ogona kapena ma restaurants) ungawononge AOI.

Mukasiya kugwira ntchito ku kampani, musatenge uthenga wa chinsinsiwu kuchokera ku AOI ndi kuulura kwa amene tima panga naye mpikisano, wolembedwa ntchito wa tsopano, kapena munthu wakunja kapena bungwe.

Tonse timasunga uthenga pamene tikugwira ntchito. Mwachitsanzo, zokhudza chuma, za makawunti, ma pulani a bizinesi, ma regulatory submissions ndi ma lipoti ofotokoza mmene ndalama zayendera. Anthu ambiri mkati ndi kunja kwa kampani amadalira kuti zimene tasungazi ndi zowona.



## Zowona za lipoti ya za Chuma (Kupitiriza)

Ndi udindo wanu kutsatira malamulo a kampani ndi ndondomeko ndikupereka uthenga wowona wonse wofunikira panthawi yake ndi womveka bwino.

AOI yakhazikitsa ndondomeko zowona ma akawunti kuti iteteze katundu wa kampani ndikuwonetsetsa kuti uthenga wa za chuma ndi wowona komanso wofunikira. Malamulo awa akuyenera kutsatidwa ndi aliyense:

Pasakhale chinsinsi pa ndalama zimene sizinalembedwe mu ma buku, katundu kapena ndalama zimene zagwira ntchito.

- Musalephere kusunga zolembeledwa, katundu ndi ndalama za kampani zimene zagwira ntchito.
- Musasunge zabodza kapena zolembedwa za kampani za bodza.
- Musapange zinthu zokopa, zonyengerera, kapena zosokoneza Accountant pamene iye akupanga audit ma statement za chuma.
- Musalipire mmalo mwa kampani ndi chikhulupiliro chakuti ndalamazo zigwiritsidwa ntchito yina yosiyana ndi imene ikuyenera kugwira.
- Nenani (mwa chinsinsi ngati simukufuna kudziwika) kwa CCD, kapena komiti ya Audit madandawulo anu ena onse okhudza za ma akawunti kapena auditing.

Kuti mudziwe ngati uthengawu ndi wowona, ukuyenera kuwonedwa ndi ma auditor, komanso wogwira ntchito m'boma. Musasiye kulondola ndondomeko za boma potolera uthenga wolondola. Musalole supavayiza kapena wogwira naye ntchito kuti atero. Kusatolera uthenga wowonawu molondola kungathe kupangitsa kuti akupatseni disipulini kapena kuti akuchotseni ntchito. Ndi udindo wawolembedwa ntchito aliyense kupanga zomwe wapemphewa ndi a oditi.

## Kupereka uthenga kwa anthu

A Chief Executive Officer, kapena amene awasankha, ndiwololedwa kuyankhula mmalo mwa AOI ndi kukonza kapena kutulutsa zotsatira za chuma cha AOI. Zonse zopempha zokhudza kampani kuchokera kwa ma analisti, ma sheyahoda, atola nkhani zipite kwa a Director of Investor Relations. Kutulutsa uthenga wa kampani kudzera mu njira zina ndi kuphwanya lamulo la kampani. Ofalitsa nkhani kapena anthu ena akafunsa zinthu zina zokhuza kampani monga ngati kampani yimatsatira malamulo a boma, kagwiridwe ka ntchito pakampani kapena zina zotero atumizidwe kwa a Manejala Oyankhula mmalo mwa Kampani. Kuwuza anthu zokhudza kampani ndi kuswa malamulo a Kampani.



## Chipepeso ndi ma benefiti

Zochitika mu payroll ya kampani ndi mapulani ama benefiti amene apangidwa kuti agwirizane ndi malamulo oyenera a boma okhudza ma ola ogwirira ntchito, malipiro, kulandira ma benefiti, kusunga zimene zalembedwa ndi zofunikira ma notisi. Izi ndizosiyana ku Amerika ndi mumayiko ena amene amachita nawo bizinesi. Kusintha kuli konse kwa zochita za kampani, mapulani ndi malamulo popanda kufunsa a Director of Human Resources a AOI ndi kulakwira malamulo a kapani.

## Kusasalana, Mwayi wosasiyana ndi Kusasalana

Kampani ndi yodzipereka kuti pasakhale kusasalana pa mwayi wantchito wosasiyana. Wogwira ntchito wonse ndi wofuna ntchito sadzasalidwa, kuzunzidwa chifukwa cha fuko, mtundu, chipembedzo,wamkazi kapena wamamuna, momwe amadziwonera ngati wamkazi/wamamuna, kukwatira kapena ayi, zokhudzana ndi zogonana, kochokera, zaka, kukhalitsa mu dziko, kukwezedwa pa ntchito, disipulini, maphunziro, malipiro ndi zonse zokhudza ntchitoyo

Chifukwa boma la Amerika limatenga kampani kukhala "kontilakita wa boma" pa zifukwa zina kampani ikuyenera kupereka mwayi wosasiyana ndi kusazunzana popereka ma kontilakiti a boma.

Tikuyembekezanso kuti alendo athu awonetsanso khalidwe limeneli, komanso wogwira ntchito, makasitomala ndi ma sapulaya pogwira ntchito yathu.

Kukakamiza munthu kugonana naye ndikoletsedwa ndipo sikudzaloledwa. Izi zikuphatikizapo kukakamiza kugona ndi munthu, pomuwuza kapena kumukakamiza, kumuwuza kuti mumukweza pa ntchito, malipiro, ndikumupatsa ntchito zina mukagona naye; kumugwira munthu malo olakwika; kuyankhula zogonana, zolaula; ndi zina zimene zingapangitse kuti malo ogwirako ntchito akhale owopsa, ovuta kapena okwiyitsa.

Ogwira ntchito adzatsatira malamulo owona za ogwira ntchito ndi zozunzana kumalo a ntchito. Wogwira ntchito amene azizunza anzawo adzaweruzidwa. Wogwira ntchito amene awona kuti akuzunzidwa akuyenera kupereka madandawulo awo kwa woyimilira wa ku human resource ndipo angawuze a Director of Human Resources a AOI nthawi yina yili yonse.



## Kuthandiza pa kafukufuku pamene walakwa

Ndi lamulo la kampani kuthandizira pa kafukufuku wochitidwa ndi a boma pa za u chigawenga kapena katangale. Kafukufu akuyenera kukhala ndi wamkulu woona za Malamulo. Musayankhule ndi wogwira ntchito M'boma pokhapokha wamkulu wa Malamulo akhalepo. Mufunse chiphaso cha wogwira ntchito m'boma ndipo musaulule zinsinsi za kampani pokhapokha akhale ndi chilolezo cha ku khoti. Wogwira ntchito m'boma angathe kufunsa za mapepala ndi zolembera atatenga chilolezo cha ku khoti (kapena kuti chisamani). Ngati wofufuza wa boma watenga katundu wa kampaniyu, Kampani isunge kalembera wa katundu amene watengedwa. Ngakhale zili chonchi, mukuyenela kuwuza wamkulu wowona za Malamulo kapena CCD

Aliyense wowona za malamulo kapena woyimira boma amene akufuna kudziwa za kampani awuzidwe kuti kampani idzagwira nawo ntchito,pokhapokha ngati wamkulu wowona za malamulo wa kampaniyi kapena CCD wawuzidwa kuti awunikiridwe mmene angayankhire.

Powonjezera ku kafukufuku wa boma, Dipatimenti yowona za Corporate Compliance idzapanganso kafukufuku wake. Wogwira ntchito wonse akuyenera kuchita mmene awuzidwira pamene kafukufukuyu akuchitika. Kuti mudziwe zambiri wonani Malamulo a zakafukufuku wa mkati wa kampani pa dziko lonse lapansi.

Pasapezeke, dayilekitala, ofisala, wogira ntchito kapena wothandizira kampani asabwezeredwe popeleka uthenga wowona wokhudza Commission pamene yalakwa. Mowonjezera, ndikuphwanya Malamulo a kampani osabwezera pamene wogwira ntchito wanena madandawulo okhudza Malamulo ndi chikhalidwe.

## Kasamalidwe ka Zolembedwa

Kampani yayamba kulondola Pulogalamu yosunga zolembedwa kuti zisungidwe mwadongosolo, zitetezeke ndikusungidwa bwino. Zolembedwa za kampani zisungidwe bwino mogwirizana ndi Malamulo, kukwaniritsa zolinga za bizinesi ya kampani ndikusungidwa monga mwamalamulo chifukwa zidzafufuzidwa ndi boma, zisamani ndi zina



zokhudza kasungidwe ka zolembedwa. Kuti mudziwe zambiri, ndipo kuti muwunikire za *Ndondomeko ya kasamalidwe ka Zolembedwa,* wonani za malamuo a kasamalidwe a zolembedwa, kapena fusani wamkulu wowona za Malamulo

## Kugwira ntchito ku malo athu

### Malo a ntchito opanda mankhwala

Kampani idzaonetsetsa kuti ogwira ntchito ake sakugwiritsa ntchito mankhwala oledzeretsa pa malo ogwilira ntchito. Pa chifukwa ichi kampani yakhazikitsa chilinganizo chodziwitsa anthu za makhwala ozunguza bongo.

Kampani ikutsatira ndondomeko ya Drug Free Awareness Act of 1988 ("'DFWA"'), limene limanena kuti kampani ikuyenera kukhala ndi malo amene sikukupezeka mankhwala ozunguza bongo ndikukhazikitsa ma pulogalamu owonetsetsa kuti izi zikukwaniritsidwa. DFWA imaletsa kupanga, kugawa, kukhala ndikugwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo ku malo ogwirako ntchito. Kutsatira za DFWA ndi udindo wa kampani kuti ithe kugwira ntchito molingana ndi mgwirizano ndi boma.

Aliyense wogwira ntchito ali ndi udindo kuwuza woyimilira depatimenti yolemba anthu ntchito kapena Mkulu wa depatimenti imeneyi wa AOI mu masiku asanu (5) amene mwawona munthu akugwiritsa ntchito mankhwalawa --- zikukhudza iwowo kapena wogwira naye ntchito --- kuchokera pa zina zimene zinachitika ku malo ogwila ntchito. Kulakwira udindowu kungapangitse kuti muweruzidwe kapena kuchotsedwa ntchito.

### Zaumoyo ndi chitetezo

Umoyo ndi chitetezo cha ogwira ntchito ndi zofunikira kwambiri ku kampani kotero kuwopsezana, kulusa, komanso mchitidwe wachisokonezo sizololedwa. Ndi lamulo la kampani kuti malo ogwirako ntchito akugwirizana ndi malamulo a dziko ndi malamulo a za umoyo ndi chitetezo cha wogwira nchito ake.

Wogwira ntchito amene angaphwanye malamulo amenewa sakuyika pa chiwopsezo moyo ndi chitetezo chawo chokha, komanso umoyo ndi chitetezo cha anzawo ogwira nawo ntchito. Pa chifukwa ichi, aliyense amene angalakwire malamulowa adzaweruzidwa.



## Kugwiritsa ntchito ana, Kukakamiza kugwira ntchito ndi maufulu ena

**Kugwiritsa ntchito ana, Kukakamiza kugwira ntchito ndi Maufulu ena**

Alliance One ndiyodzipereka kuthetsa mchitidwe wogwiritsa ntchito ana, kukakamiza kugwira ntchito ndi machitidwe ena oyipa okhudza kagwiridwe kantchito, kukapezeka kuti machitidwe otero alipo ndipo idzawonesetsa kuti maofesi ake onse akhale ndi kakhalidwe kabwino kakagwiridwe kantchito. Kudzipereka kwa Kampaniyi pantchito yothetsa makhalidwe oyipawa kukuwonekera pa malamulo ake a Kagwiridwe Kantchito Paulimi komanso Lamulo Loletsa Kugwiritsa Ana Ntchito, malamulowa akhoza kupezeka pa intraneti komanso pa webusayiti ya kampaniyi pa www.aointl.com.

Ndi lamulo la AOI kugwira ntchito mogwirizana ndi malamulo a m'dziko a za chilengedwe kuti asamale ndi kuteteza chilengedwe. Powonjezera pamenepo, kampani ikuyesetsa kutenga nawo mbali mu zochitika zothandiza kusunga chilengedwe. Mukuyenera kutsatira malamulowa ndipo wuzani a CCD, ngati muli ndi mafunso kapena madandaulo okhudza za chisamaliro cha chilengedwe.

### Kugwira ntchito kumalo a msika

AOI imapanga bizinesi pa dziko lonse la pansi. Nthawi zina zimene zingachitike mu dziko lina zingathe kuyika kampani kukhala pansi pa malamulo a dziko lina maka pansi pa malamulo a boma la Amerika.

## Kudana ndi Kunyanyala

Kunyanyala ntchito/bizinesi kumachitika pamene munthu, gulu, kapena dziko lakana kupanga bizinesi ndi anthu kapena mayiko. Lamulo la ku U.S. lodana ndi kunyanyala ntchito/bizinesi limaletsa ma kampani a ku U.S. ndi ma bulanchi awo kugwirizana ndi kunyanyala kwina kuli konse, pokha pokha ngati kwavomerezedwa ndi boma la U.S (mwa chitsanzo, ziletso pa za chuma zoyikidwa ndi a UN). Ma kampani a ku U.S ndi ma bulanchi awo akuyenela kuwuza boma la U.S. zilizonse zimene akufuna kuti anyanyale nawo.



## Zoyenera kupereka pamene kampani yalakwa

Ngati mwanamiza kapena kupanga chinyengo munthu wina kapena bizinesi mukuphwanya malamulo ambiri ochitira bizinesi a AOI. Mwa chitsanzo, kusafotokoza bwino za maonekedwe a fodya, mulingo wa zinthu kapena ziphaso zopelekedwa kwa makasitomala, malipoti ku boma kapena ma dokumenti aza zotumizira katundu kapena ku banki zingathe kuwonetsa chinyengo kapena zolakwa zina. Komanso, kukambirana zoterozo pa ma foni, facsimile, makalata a pa makina, oposita zingatanthauze chinyengo.

Malamulo a Amerika pa za chinyengo amafika patali ndipo wolakwira malamulowa adzapatsidwa fayini ndi kumangidwa chifukwa chophwanya malamulowa. AOI ikuletsa mchitidwewu ndipo ikuyembekeza kuti wogwira ntchito ake atsatira malamulowa.

Powonjezera Malamulo odana ndi uchigawenga, Kampani idzakhuzana ndi zoyenera kupereka pamene yalakwa, kuphatikizapo kulowerera ma kontilakiti a bizinesi, kusokoneza uthenga wa bizinesi ina, kukopera katundu wa ena, ndi kuononga mbiri ya ena . Choncho ndikofunikira kunena zoona pamene mukukamba za kampani, ma kampani ena ndi anthu ena, ndikusalakwira ufulu wa ena kudzera mu dzina la kampani.

## Kuba Ndalama

Kuba ndalama kumachitika pamene munthu atenga zimene wazipeza atalakwa kuti ziwoneke ngati sizinapezeke munjira yolakwika. Malamulo a mu mayiko ambiri amaletsa dala kugwiritsa ntchito zinthu zimene zapezeka munjira yolakwika.

- Mukuyenera kutsatira malamulo onse amene akukamba za kuba ndalama ndi malamulo amene akufuna kuti inu munene pamene mwaona ndalama ndi zinthu zina zolakwika.
- Mukuyenera kupeza zokwanira pa makasitomala, ma sapulaya ndi ena amene mukuchita nawo bizinesi kuti mudziwe kumene ndalama zawo zikuchokera kumabizinesi ovomerezeka.
- Mukuyenera kutsatira malamulo onse okhudzana ndi ndalama. Ndi zosavomerezeka ndi malamulo a kampani kulandira ndalama ndi ma invoice. Ndipo ndi zosavomerezeka ndi lamulo la kampani, pokha pokha ngati pali china chake ndiponso ndi ulangizi wa zamalamulo wa kampani, kulandira ndalama monga ngati ma money order kapena ma travelling cheque kapena kulandira ndalama kwa amene simukumudziwa. Ngati ndalama zoterozo ndizovuta kuzipewa mulandire chilolezo kuchokera kwa Ofisala wa ku kampani ndikutsatila zonse zimene zikugwilizana ndi malamulo a United States Internal Revenue Service.



- Mukuyenera kuwonetsetsa kuti makasitomala wonse, ma sapulaya, ndi ena wonse amene mumachita nawo bizinesi ali wololera kusunga zonse zoyenera ndikupereka malipoti.
- Mukuyenera kukhala tcheru pamene ndalama zikuperekedwa ndipo zikuwonetsa kuti ndizobedwa, monga:
    - Ndalama kapena zopereka zodabwitsa;
    - Kubweza ngongole mwansanga;
    - Kuwoda kapena kugula katundu kapena zochitika zina zowoneka zodabwitsa ndi bizinesi ya kasitomala wanu;
    - Kupereka ndalama kodabwitsa, ndi kaperekedwe ka ndalama kodabwitsa;
    - Kupereka kuchokera kwina kupita kwina zodziwika kuti ndi misonkho ya ku madera kwina yotchedwa “tax haven” ndipo zikugwirizana ndi kuba ndalama
    - Kufunsidwa kupereka ndalama kwa munthu kapena akawunti yosadziwika.

## Kudana ndi kusakhulupirika ndi mpikisano wosakondera

Pa dziko lonse lapansi, zochitika za bizinesi ya AOI zikuyenera kutsatira malamulo odana ndi kusakhulipilika ndi mpikisano wosakondera wa mayiko osiyana siyana. Ku Amerika, lamuloli limatchedwe Sherman Act, limaunikila zilango pamene palakwikwa ndi zimene kampani ikuyenera kupereka pamene yalakwa. Zilango za mu Sherman Act padziko lonse la pansi ndi zazikulu. Kulakwira Sherman Act kungathe kupangitsa kuti akumangeni kwa zaka khumi ndikupereka US$1,000,000.

Malamulowa alipo kuti alimbikitse mpikisano. Akuletsa mgwirizano kapena zochitika pakati pa opanga mpikisano amene amatha kuletsa malonda kapena



kuchepetsa mpikisano. Migwirizano ndi zochitika zimene ziri munsizi ndi kuphwanya malamulo:

- kukonza kapena kuwongolera mitengo yoperekedwa kwa masapulaya kapena makasitomala pa amene akupanga mpikisano.
- Kupereka zinthu kumadera kapena misika;
- Kunyanyala kwa gulu: kugwirizana ndi opikisana nawo kuti munyanyale ma sapulaya ndi makisitomala ena.

Nkofunikira kuona mgwirizano pakati pa opikisana umene ukulakwira malamulo odana ndi kusakhulupirika asakhale mu mgwirizano, koma afotokozeredwe mwa kachetechete pamene pali umboni ndi pamene akuchita zosiyana ndi izi. Nkofunikira kuchita mogwirizana ndi malamulowa kuti mupewe kukolana ndi opikisana nawo pokhudza mitengo, zoyenera kutsatira pogulitsa, ma dera, ma kasitomala, ma sapulaya, kapangidwe ka katundu ndi zina za mu mpikisano zimene zingagwire ntchito ngati umboni. Pali chiopsyezo ngati malamulo odana ndikusakhulupirika akukhudzana ndi mitengo ya opikisana nawo, koma nthawi zina izi ndizololedwa. Musanapereke uthenga wa mitengo kwa amene mukupikisana nawo, wuzani wamkulu wopikisana nawo kuti akuwuzeni zambiri zokudza izi musanapitirize kupanga izi.

## Mchitidwe umene ungaphwanye Malamulo odana ndi Kudana ndi kusakhulupirika

Pamene zochitika zina ngati zimene zili pamwambapa, ndizolakwika ndi zoletsedwa, zina ndi zolakwika pokhapokha ngati kupikisana kwawo sikukubweretsa phindu liri lonse ku mpikisano. Mukuyenera kuwuza wamkulu wowona za Malamulo, CCD musachite nawo zochitikazi:

- Kuchita pamodzi: kumene kumachitika pamene wogula agwiritsa ntchito mphamvu zake zogula pogulitsa ku ma sapulaya ake;
- Kuchita payekha kumene kumachitika pamene wogula wavomereza kugula katundu yense kuchokera ku wogulitsa mmodzi;
- Mgwirizano wopingasa umene umachitika wogulitsa ali ndi mphamvu pa katundu amene wogula akugula;
- Mgwirizano wochita kupangidwa zogula ndi mabizinesi ena;



## Kudana ndi kusakhulupirika ndi mpikisano wosakondera

(Kupitiriza)

- Kuvomereza chinthu, kapena kuvomereza wogwira ntchito wina kapena ofisala wa kampani kuvomereza chinthu, pa ma dayilekitala a kampani ina;
- Kufunsa ma kasitomala kugula katundu ndi ma service pamodzi ndi zina kapena kutsitsa katundu amene wagulidwa kapena ma service amene agulidwa kale;
- Kupereka layisensi ndi zipangizo zina zimene zikuchepetsa ufulu wa amene akupereka layisensi ndi amene akuyilandira.

### Kusalana pa Mitengo ya zinthu.

Malamulo oletsa kupondereza pa mitengo ya zinthu pamene anthu ogula awiri akupikisana, ngati mtengo ukupangitsa wina kukanika kupikisana nawo. Kupereka ndalama pa nthawi ya kulengeza malonda nkoletsedwa ngati kukanikitsa kasitomala wina kupikisana nawo. Kusiyana kwa mitengo nkololedwa nthawi zina ngati kuli kofunikira ndipo kukukwaniritsa (osati kupitilira) mtengo wa amene akupikisana nawo. Komano, musafananize mitengo ya amene mukupikisana nawo pachifukwa chimenechi.

### Kuphangira

Pamene Kampani ili ndi mphamvu kwambiri ndipo ikuwonetsa “mphamvu zochuluka kwambiri kumsika” ndipo ikukonza mitengo ndikuletsa kupikisana, ikuyenera kufufuzidwa kuti muwone kuti mphamvuzo ikuzitenga kuti ndipo ikuzigwiritsa ntchito bwanji phamvu zakezo. Ngati dera lanu liri ndi mphamvu zochuluka kwambiri ku msika, ngati kukhala nokha wogula kapena kuperekera fodya, pewani khalikdwe lokonza mitengo ndikuletsa kupikisana, ngati kuchita moletsa wopikisana nawo kuchita nawo bizinesi. Wuzani wamkulu wowona za Malamulo, CCD ngati muli ndi mafunso pa kuphangira ndi pamene mukuwona kuti muli ndi mphavu zochuluka ku msika.

Kuphangira kungathe kuchitika pamene ma kampani woposa awiri akumana kuti akhale ndi mphamvu yokonza mitengo ndikuletsa kupikisana. Madandaulo a zimenezi apite kwa wamkulu woona za Malamulo, CCD izi zisanachitike.



## Mabungwe a Zamalonda

Zochitika mogwirizana sizizalekeka chifukwa zikudzera ku ma bungwe a malonda. Mukhale wosamala pamene mukutenga nawo mabali mu bungwe la malonda, potsatira Malamulo ali pamwambawa pamene mukuyankhula ndi opikisana nawo. Powonjezera pamenepo, musakhale m' bungwe la malonda limene limaphwanya Malamulo oletsa kupikisana, chilango chidzaperekedwa kwa ma membala amene adzachite nawo malonda mophwanya Malamulo. Ngati muli ku msonkhano wa bungwe la malonda limene akukambilana zoletsa mpikisano ndikuphwanya malamuo ena, muchokepo mwansanga ndikunena izi kwa wamkulu wowona za Malamulo, CCD.

Uzani wamkulu wowona za Malamulo, CCD ngati mukutenga nawo mbali m' bungwe la malonda limene limawona za pulogalamu ya kalembera, mitengo ya zinthu, kachulukidwe ka katundu amene wapangidwa, mitengo, katundu amene alipo ndi zina zambiri zimasindikizidwa kuti muthe kumvetsetsa mmene chuma chikuyendera. Mapulogalamu oterewa ndiwovomerezeka ngati zonse zoyenera kulondolezedwa zatsatiridwa.

?

*Kodi Mukudziwa?*

*Ngakhale mabungwe a malonda ali othandiza nthawi zina, amapereka ziopsezo ndi opikisana nawo ndikupereka uthenga umene ungasokoneze mpikisano pa msika. Ndikofunika kufuna wamkulu wowona za Malamulo, CCO kapena CCM musanalowe m' bungwe a malonda*

**Malamulo owona za kutumiza katundu olowa kapena kutuluka**

Nthawi zambiri, boma limapereka ziletso pa malonda/kayendedwe ka katundu wolowa ndikutuluka kupita ku mayiko akunja. Mwachitsanso, Malamulo a ziletso pa malonda a ku U.S amaletsa anthu aku U.S kuchita bizinesi ndi anthu amene ali ndi ziletso pa malonda, sakuyenera kuwagulitsa zinthu, kapena kuwagula zinthu, kutumiza ku U.S kapena kulumikizana ndi mayiko amenewa. Ndi lamulo la kampani kugwirizana ndi malamulowa amene amapezeka mu mayiko ena. Chonde wonani Malamulo a kampani wowona za zilesto pa malonda ndi Malamulo a Summary of United States Economic Trade Sanctions kuti mudziwe zambiri, ndipo wuzana CCD ngati muli ndi mafunso okhudza ziletso pa malonda.

Maka maka, wogwira ntchito kapena wothandizira sakuloledwa kulipira mayendedwe a zinthu kapena kasitomu popanda CCD kudziwa.

Zochitika pansipa zikuyenera kuwonedwa:

- A Boma la Amerika ndi mayiko ena ali ndi malamulo ofuna kuti mulembepo pa malondapo kumene akuchokera. Mukuyenera kutsatira izi ndi malamulo ena olemba pa katundu.
- Kampani itha kukhala ndi zokhoma “drawbacks” pokhudzana ndi katundu wolowa ndi ndalama zoperekedwa mokhudzana ndi malamulo. Muwonetsetse kuti zokhomazi “drawbacks” sizili ndi ma mawu a bodza kapena chinyengo.
- Musatenge nawo mbali pophwanya malamulo ndikupereka ziphuphu
- Musakonze ma invoice a kampani a chinyengo pa zinthu zimene zagulitsidwa.
- Masatifiketi olakwika mogwirizana ndi za katundu wotuluka kapena makalata angongole
- Kupereka zolembedwa zolakwika pa zimene ochita malonda apempha.
- Kusintha zinthu zimene sizili mu invoice kapena zolembedwa zina
- Kuchita bizinesi ndi makasitmala a tsopano.



## Malamulo athu mwa chidule

AOI ikudalira inu kuti mupanga zomwe za lembedwa mu malamulowa. Zili munsizi zikuwonetsa mwachidule mmene mungagwirire ntchito molingana ndi malamulowa.

*Dziwani ndi kuchita monga mwa malamulo.* Podziwa ndikumvetsetsa ndikulondola malamulo a kampaniwa ndi zimene zingatipangitse kukhala a chitsanzo.

*Dziwani lamulo ndikufunsa mafunso.* Mukuyenera kudziwa malamulo amene akukhudzana ndi ntchito ndi udindo wanu. Ngati simukudziwa lamulo la kampani, ngati lilipo, funsani a CCO kapena CCM a kampani yanu.

*Musamangoganizira zinthu.* Musaganize kuti akulu akulu akudziwa kapena sakusamala za chinthu china choncho muyenera kufunsa kuti mudziwe. Komanso, musaganize kuti china chake sichikonzedwa. Akulu akulu a AOI ndi wodzipereka kuwonetsetsa kuti za malamulo zimene zikuyenera kuchitika zikutsatidwa. Tifuna mutiwuze ngati pena palakwika.

*Musangoyang'anira zolakwikazi, Mukanene.* Tikuyenera kuyika pa mtima malamulo akampani. Ngati mukuwona kuti wina akuphwanya malamulowa, tsatirani njira zoyenera kuti muzikonze. Nenani kwa CCD a kampani kapena kwa Manijala wowona za Compliance wa mu dera lanu, wowona za Audit mu bodi ya ma dayilekitala kapena yimbani foni panambala ya ulere (mobisa ngati simukufuna kudziwika)

*Musakakamizidwe.* Sikololedwa kuphwanya lamulo, kapena kukakamizidwa kuti mutero – ngakhale kuphwanya lamulo kungathandize kuti mukwaniritse zolinga zanu.

